UFULU NDI SANKHO
VUTO YA AZIMAI MU ZAMBIA

Naomi Njobvu

(CiNyanja/CiCewa)

Monograph Series No. 260
Centre for Advanced Studies of African Society (CASAS)

R100
3/16

UFULU NDI SANKHO
VUTO YA AZIMAI MU ZAMBIA

Naomi Njobvu

(CiNyanja/CiCewa)

Centre for Advanced Studies of African Society (CASAS)
P.O. Box 359
Rondebosch, 7700
Cape Town, South Africa
CASAS Publications can be ordered from our website www.casas.co.za

© The Author

HQ
1236.5
.Z33
N56
2015

First Published 2015

ISBN 978-1-920287-93-1

All rights reserved. No part of this publication may be reproduced, stored in a retrieval system, or transmitted in any form or by any means, electronic, mechanical, photocopying, recording, or otherwise, without prior permission of the copyright holder.

This publication was printed with the kind support of the Open Society Initiative for Southern Africa (OSISA).

Printed by Dash Print

4373840

ENGLISH SUMMARY

The title of this work may be literally translated into English as *Freedom and Discrimination: The Challenges of Women in Zambia*. The work addresses the state of gender relations in Zambia and the wider southern African society in which women's rights are constrained by age-old traditions and beliefs. It is a topic with current relevance within the Zambian context where issues of women's rights are increasingly becoming crucial. The author's main line of argument is that traditional belief systems and practices have shaped people's perceptions of women and their role in society. These practices undermine the status of women and fail to accord women and girls opportunities to realise their potential by restricting their participation in politics, education and in modern careers, most of which are predicated on one acquiring a good education. The author argues for more inclusive practices in which women play a greater role in all aspects of life than is currently the case. If this happens, the author argues, it will lead to greater well-being of individuals and society at large.

MAU OYAMBA

Anthu a mmaiko ambili pa dziko lapansi amakhala akulankula pa kusiyana kumene kulipo pakagawidwe ndi kagwilidwe ka nchito pakati pa azimai ndi azibambo. Azimai amagwila nchito zimene zimachedwa zacikazi ndipo azibambo nawonso amagwila nchito zomwe amati zacimuna. Azibambo amadziwika kuti ndi anthu amphamvu ndipo amagwila nchito zolimba monga kukumba miyala pa migodi, kutema mitengo ndi zina zotelo. Azimai nawonso nchito zao ndi kufuna cakudya, kusamala nyumba zao ndi kusunga ana. Mutahhery (1992) ananena kuti anthu ophunzila ena monga *Plato* anazindikila kuti kusiyana pakagwilidwe ndi kagawidwe ka nchito pakati pa azimai ndi azibambo kunali kosayenela mpang'ono ponse cifukwa azimai nawonso anali ndi mphamvu yogwilila nchito ndi kucita zinthu zambili zimene azibambo anali kucita. Iye anaona kuti mkhalidwe wopondeleza azimai umacitika cifukwa cakuti azibambo sanali kufuna kuti mkazi akhale ndi mphavu ndiponso ufulu womwe iwo anali nawo. Iwo amaona munthu wamkazi ngati kuti ndi cinthu cao cosunga kapena tinene kuti ngati ciweto cao. Cifukwa ca maganizo otele pakati pa azibambo, anthu ambili anaganizapo nayamba kukambilana ndi kulemba nkhani ndi mabuku onena za kusiyana kumene kulipo pakati pa azibambo ndi azimai. Ngakhale *Aristotle* anavomeleza zimene *Plato* analemba, kuti azimai anali ndi nzelu zolingana ndi azibambo ndipo angathe kugwila nchito zimene zinali kuchedwa zacimuna. Iye anatsimikiza kuti kusiyana pakati pa azibambo ndi azimai kunalipodi cifukwa cakusiyana kwa kalengedwe ka matupi awo. Iye ananena kuti, azimai ali ndi mathupi ofewa ndipo osalimba koma azibambo ali ndi mathupi olimba. Ananenanso kuti kusiyana kumapezekanso pa luso lopanga zinthu ndi nchito zimene mitundu iwiliyi imafunika kugwila.

Gyimah (2009) anaona kuti panalibe phindu kuti mzimai akhale wopondelezedwa panchito ndi panyumba. Cifukwa ca ici, iye anayamba kulankhula pa ubwino woti azimai akhale ndi ufulu ndi mutendele wogwila nchito zimene azibambo anali kugwila mmalo osiyanasiyana mu umoyo wao. Pepala limeneli lalembedwa kuti lisonyeze kusiyana kumene kulipo pa kakambidwe, kalembedwe, kagawidwe ka nchito ndi kacitidwe kazinthu pakati pa azimai ndi azibambo mmalo monga, mmasukulu, mzipatala, mmidzi, pamiseu ndi malo ena ambili padziko lapansi makamaka mdziko la Zambia. Ponena zakusiyana kumeneku tidzayesanso kuonetsa kusiyana kwa ufulu ndi mtendele pakati pa azimai ndi azibambo mmaiko ndi mumakontineti ena pa dziko lapansi. Potsiliza, tidzakamba za ubwino

umene dziko la Zambia lingapeze ngati lipitiliza kupatsa azimai mphamvu ndi ufulu wocita zinthu ndi kugwila nchito zimene azibambo amagwila.

UFULU WACIBADWIDWE

Ufulu ndi cinthu cofunikila kwambili pa dziko la pansi makamaka pakati pa azimai ndi azibambo. Anthu amene ali ndi ufulu wa cibadwidwe sapondelezedwa ndi anthu anzawo kapena boma limene lili pa ulamulilo ngati iwo akudziwa kufunikila kwa ufulu umenewu. Anthu amene amadziwa kufunikila kwa ufuluwu amathandiza dziko lawo kukhala mwa mtendele. Ici cimasonyeza kuti ufulu ndi mtendele zimayendela pamodzi kuti dziko litukuke. Ncifukwa cake sipafunika sankho pakati pa azimai ndi azibambo pa kagwilidwe kanchito kapena kakambidwe kamaganizo kuti dziko lililonse litukuke. Mmaiko ambili, azimai amapambana azibambo pakuculuka ngakhale kuti iwo amapeza mavuto osiyanasiyana kupata ufulu. Mavuto amenewa sapezeka mmaiko osauka okha komanso mmaiko olemela. Monga ananenela Tiondi (2001) "azimai ndiwo amalima cakudya cambili padziko lapansi. Mwacitsanzo, m'madela a ku *mwela kwa Africa* ndi ku *Caribbean*, azimai amalima cakudya cokwanila 80% cofunikila mmabanja awo. Ku *Asia*, azimai ndiwo amalima ndi kukolola cakudya cokwanila 50%. Kudela la *Latin America*, azimai amalima cakudya cokwanila mumabanja awo ndipo amasunga nkhuku ndi ziweto zina." Koma ngakhale zili tele, azimai sapatsidwa cithokozo comwe iwo amayenela. Ndiponso, nthawi zina, azimai sapatsidwa malipilo alionse panchito imene amagwila ndipo ngati apatsidwa malipilo, malipilowo amakhala ocepela kwambili kulingana ndi nchito yomwe iwo amagwila. Ngakhale zonsezi zimacitika tele, azimai ambili sadziwa kuti kuli mabungwe amene iwo angapiteko kukadandaula cifukwa ambili mwaiwo sadziwa za ufulu wacibadwidwe umene ali nawo.

Vuto lina limene azimai amapezana nalo ndilakuti samapatsidwa thandizo lokwanila monga ngati zipangizo zolimila ndiponso mbeu zoti abyale ngakhale kuti iwo ndi amene amagwila nchito ya ulimiyi. Shuh (2010) ananena kuti azimai ndi atsikana amagwila nchito kupambana azibambo koma malipilo awo amakhala ocepa kwambili kotelo kuti m'malo moti umoyo wao upite patsogolo, iwo akhala ovutika ndi kusauka pa umoyo wao wonse. Zonsezi zimacitika cifukwa azimai ambili sadziwa kuti ali ndi ufulu wodandaula ngati sanakondwele ndi malipilo kapena makambidwe a anthu pa nchito yao. Kusiyanitsa kagawidwe kanchito

pakati pa azimai ndi azibambo kumasowetsa ufulu ndi mtendele woti azimai akhale ndi zinthu zaozao zoti zingawathandize kusunga mabanja awo ndi kukhala ndi umoyo wa bwino.

Kusiyana kwa kagawidwe kanchito ndipo kusowa kwa ufulu kumene kulipo pakati pa azimai m'madela ambili padziko lapansi kumapezekanso pakati pa asilikali. Mmaiko ambili Mkulu wa asilikali amakhala mwanuna kapena cifukwa cakuti azimai amadziwika kuti ndi anthu ofoka ndiponso kuti okonda kukambakamba kotelo kuti sangathe kugamula mlandu kapena kusunga cinsinsi ca dziko lao. Chambers (2002) analemba kuti azimai ndi anthu amene amadziwika kuti ndi amulomo, okambakamba kotelo kuti amafunika amuna olimba kuwakwanitsa. Ici cimasonyeza kuti mutundu wa azimai unapatulidwa kale ndi mwambo wa makolo kukhala mtundu wokambakamba. Ncifukwa cake azibambo amapatsidwa udindo wotsogolela anzao panchito zoteteza maiko ao. Kambili azimai amapatsidwa udindo wapansi ndipo samaitanidwa mmene aitanila azibambo amene ali ndi udindo wolingana ndi wawo. Mwacitsanzo, ngati msilikali wacimuna ndi sajenti, amaitanidwa kuti sajenti cabe. Koma ngati sajenti ndi mkazi, amaitanidwa kuti sajenti wamkazi. Cimodzimodzi *kapokola* wamwamuna ndi *kapokola* cabe, koma ngati ndi wamkazi amaitanidwa kuti kapokola wamkazi. Kusiyanaku pakaitanidwe ndi njila imodzi yofuna kusonyeza kuti pali kusiyana pakati pa azibambo ndi azimai ndiponso kuti kusiyanaku kumapezekanso mmalo anchito. Simwinga (2006) anapatsa zitsanzo za mmene anthu amaitanila mfumu yacikazi mu ciTonga kuti *Sibbuku Mukaintu*. Citsanzo ici cingayelekezedwe ndi m'mene Angoni a ku Chipata amaitanila mfumu yacikazi, kuti *mfumukazi*. Kenaka, kuitana anthuwa motele nkufuna ndithu kuonetsa kusiyana pakati pa azimai ndi azibambo.

Malo ena amene sankho limapezeka mkaitanidwe ka anthu ogwila nchito ndi mzipatala. Kalelo adokotala anali amuna okhaokha mmaiko ambili. Koma popeza kuti nthawi ino tili ndi adokotala akazi, anthu sanena cabe kuti adokotala koma amati adokotala akazi a uje, nachula dzina. Cikhulupilo ceniceni cakuti dokotala wamkazi angagwile nchito kulingana ndi dokotala wammuna palibe. Anthu ambili amafuna kuonedwa ndi dokotala wammuna ngati iwo adwala. Cimodzimodzinso, nchito ya unasi inali kugwilidwa ndi azimai mzipatala. Koma masiku ano, mzipatala mumapezeka manasi amuna. Nawonso amuna saitanidwa cabe kuti anasi, koma anasi amuna kusonyeza kuti nchito imene iwo amagwila ndi nchito yogwila akazi. Kakambidwe kotele ndi njila imodzi yofunitsitsa ndithu

kusonyeza kuti pali kusiyana pa nchito za azimai ndi nchito za azibambo. Ici cimasonyeza kuti mau amene anthu amagwilitsa nchito pofuna kunena za nchito za azimai kapena azibambo nawonso amasonyeza sankho. Tinganene kuti mau nawonso ali ndi mphamvu zodyetsa sankho pakati pa azimai ndi azibambo. Mhute (2008:60) mu pepala lomwe analemba lochedwa *Language and Gender* nayenso anasonyeza kusiyanaku poyelekeza mmene maiko apadziko lapansi amaitanidwa. Iye anena kuti maiko ambili pa dziko lapansi amadziwika ndi mlowa malo wacikazi womwe uchedwa '*she*' mcingelezi, kusonyeza ulemu umene anthu akazi amapatsidwa. Izi zikutsutsana ndi zinthu zimene zimacitika pa umoyo wa azimai cifukwa amene amalamulila maiko ambili ndi azibambo osati azimai. Zonsezi zikusonyeza kupondelezedwa ndi kusazindikila ufulu wacibadwidwe umene azimai ali nawo mdziko lao ndiponso pa zinchito. Kusiyana pakati pa azimai ndi azibambo kumapezekanso pakalembedwe ka mabuku, makalata ndi zina zace.

Olsson (2000) anafufuza kusiyana kwa kalembedwe ka makalata acidziwitso pakati pa azimai ndi azibambo amene ali ndi udindo. Iye ananena kuti, pali kusiyana pakalembedwe ka makalata a cidziwitso pakati pa azimai ndi azibambo. Iye anati azimai amalemba makalatawa ndi ulemu wopitilila malile kupambana azibambo. Kusiyanaku kungakhale cifukwa cakuti azimai amakula ndi phunzilo lonena kuti amafunika kupeleka ulemu kwa anthu akuluakulu ndiponso kwa amuna. Izi zimapezeka kwambili mmabanja a mu Africa ndi madela ena a ku Europe. Mwacisanzo, kumwela kwa dziko la Italy, atsikana amaphunzitsidwa kuti safunika kulankhula mokuwa ndipo amafunika kugwila nchito zapanyumba monga kusesa pakhomo, kuphika ndi kusunga ana anzao, ngakhale kuti masiku ano mkhalidwe umenewu uli kusintha pang'ono pang'ono.

Kusowa ufulu wacibadwidwe pakati pa azimai kalelo kunali kupezekanso panchito yolemba mabuku ndi nkani zosiyana siyana. Akalemba akazi samaloledwa kuulula maina ao enieni posindikiza zolemba zao. Iwo anali kuwopa kuti anthu adzasula zolemba zao cifukwa cakuti nchito yolemba inali kudziwika kuti ndinchito ya amuna. Ici cikutanthauza kuti zolemba zao sizikadakhala ndi phindu cifukwa anthu sankawelenga zolembedwa zao. Azimai amaopanso kupondelezedwa ndi kunyozedwa pazolemba zao ngati anthu atadziwa kuti zolembedwazo zinalembewa ndi mkazi. Pofuna kuteteza vuto limeneli, azimai ambili anali kugwilitsa nchito maina a cibwana kapena maina acimuna. Mwacistanzo, mmodzi mwa azimai amene anagwilitsa maina acimuna pazolemba zake ndi *Anna Evans*

amene anadziwika ndi dzina loti *George Eliot*. Iyeyu analemba mabuku monga *Adam Bede* lomwe linasindikizidwa mcaka ca 1859, *Silas Marner* imene inasindikizidwa mcaka ca 1861 ndi *The Mill on the Floss* imene inasindikizidwa mcaka ca 1860 (www.webdesignschoolguide.com/.../10 famous females).

Winanso mlembi amene anagwilitsa nchito dzina lacimuna ndi *Alice Bradley Sheldon* yemwe anadziwika ndi dzina loti *James Tiptree*. Iye anacita zimenezi cifukwa zolemba zake zinakhuza maphunzilo a sayansi (*science*). Sayansi imadziwika kuti ndi phunzilo la amuna. Iye analemba mabuku monga *Birth of a Sales Man* limene linasindikizidwa mcaka ca 1968 ndi *Worm Worlds and Otherwise* limene linasindikizidwa mcaka ca 1975. Iyeyu amaopa kuti anthu akadziwa kuti ndi mkazi amene analemba mabuku amenewa, iwo adzawasula ndipo sadzakhulupilila zolemba zake. Winanso mlembi amene anasintha dzina lake ndi *Charrotte Bronte* amene anagwilitsa nchito dzina loti *Currer Bell* ndipo ndiye analemba buku lochedwa *Jane Eyer* limene linasindikizidwa mcaka ca 1859, (www.webdesignschoolguide.com /.../10 famous females).

Kusintha mainaku pakati pa alembi akazi inali njila imodzi yozibisa ku anthu owelenga kuti mabukuwo analembedwa ndi munthu wamkazi. Ngakhale zinali tele paciyambi colemba mabuku ao, patsogolo pake, anthu anadziwa maina ao azoona, ndipo anapitilizabe kuwelenga mabuku kapena nkhani zao cifukwa anali atadziwika kale kuti zolemba zao zinali zocititsa cidwi. Zitsanzo zimene zapelekedwa pamwambapa zikusonyeza kusowa cikhulupililo mwa azimai ndiponso kusadziwa ufulu wacibadwidwe umene azimai ali nawo. Cinanso ndi cakuti azimai ambili anavomela kuti mtundu wao ndi mtundu wofoka, wopanda nzelu ndipo wokonda kukambakamba zinthu zopanda mutu. Ndi cifukwa cake alembi amenewa anafuna kudziwika ndi maina acimuna. Ngakhale zinali telo, nyumba zosindikiza zolembedwa zinasunga cisinsici ndi kuthandiza azimai kusintha maina awo ndipo iwo anasindikiza zolembedwazo. Ici cinathandiza kutsegula njila yoti azimai akhale ndi ufulu wolemba ndi kutengako mbali pazocitika zina monga ndale mmaiko awo.

Ndale ndicithu cimodzi cimene anthu ambili amafuna kutengako mbali. Mmaiko ambili, azibambo ndiwo amene amatengako mbali m'ndale. Ross (2000) analemba pepala pa mkhalidwe umene ulipo pakati pa azimai ndi azibambo, pa nthawi ya ndale ndipo mmene atolankhani amacitila lipoti. Cigawo ici cinena mmene atolankhani amaitanila azimai amene amatengako mbali m'ndale nthawi ya kampeni. Iyeyu amanena kuti

atolankhani amasiyanitsa mmene amaitanila azimai ndi azibambo mu malipoti awo. Mmalo mopeleka lipoti pazinthu zenizeni zimene azimai akambapo, iwo amafunafuna zinthu zimene zilibe kumutu pofuna kupondeleza azimai. Atolankhani amakonda kulemba pakavalidwe, kapena kaonekedwe ka mkazi amene akutengako mbali mndale mmalo molemba zazinthu zimene iye wanena.

Nthawi zinanso panthawi yakampeni, atolankhani amafuna kuonetsa monga kuti matupi a azimai anapangidwila azimuna. Ngakhale kuti mkazi amazipatsa ulemu, atolankhani amacotsapo ulemu nayamba kunena zinthu zokhuza ukazi wake. Nthawi zina pofuna kugonjetsa azimai amene amakonda kusintha sintha magulu andale, iwo amagwilitsa nchito mau onena kuti ndi wodwala kapena kuti alibe mwambo. Vuto lina ndilakuti, ngakhale azimai anzao amanena mau onyoza mmalo moti ateteze anzao. Nawonso atola nkhani acikazi, sanena zinthu zabwino pa azimai amene atengako mbali mndale kapena kulamulila mdziko.

Tikaona bwinobwino za ndale mmaiko ambili, tiona kuti azimai amene atengako mbali ndiocepa kwambili. Ndi cifukwa cakenso azimai amene ali ndi udindo wa ulamulilo mmaiko ambili ndi wosakwanila makhumi atatu (30). Pamaiko okwanila 195 pano pa dziko lapansi azimai cabe okwanila 19 ndiwo ali paudindo wotsogolela maiko ao. Mu Africa, azimai osapitilila atatu ndiwo ali pa udindo wotsogolela maiko awo. Ku mwela kwa Africa, kucokela mcaka ca 2012 kufika mcaka ca 2014, dziko la Malawi ndi dziko lokha limene linali ndi mtsogoleli wamkazi. Dziko la Zambia silinakhalepo ndi Mtsogoleli wa dziko wamkazi kucokela pamene linatengela ufulu mcaka ca 1964.

MAU OBWELETSA SANKHO MNDALE MU ZAMBIA

Dziko la Zambia lili ku mwela kwa kontineti ya Africa ndipo ndilozungulidwa ndi maiko okwanila asunu ndi atatu. Maiko amenewa ndi Angola, Tanzania, Malawi, Zimbabwe, Botswana, Namibia, Mozambique ndi Democratic Republic of Congo. Dziko la Zambia ili ndi zigawo zokwanila khumi. Zigawo zimenezi ndi *Central*, *Copperbelt*, *Eastern*, *Luapula*, *Lusaka*, *Muchinga*, *Northen*, *North-western*, *Southern* ndi *Western province*. Mu Zambia muli anthu okwanila pafupifupi zikwi khumi ndi tutatu (13 miliyoni). Ambili mwa anthu amenewa ndi azimai. Ngakhale azimai ndi oculuka, azimai amene amatengako mbali mndale ndi ocepa.

Mwale (2012) analemba pepala lonena za azimai amene anasankhidwa kukhala a phungu mnyumba ya malamulo mdziko la Zambia. Azimai okwanila 20 cabe pa anthu 158 ndi amene anapatsidwa udindo wokhala aphungu mnyumba ya malamulo mdziko la Zambia. Ici cikutanthauza kuti aphungu 138 ndi azibambo. Kucepa kwa nambala ya azimai mnyumba ya malamulo kukusonyeza kuti ndale simalo kapena nchito ya azimai. Azimai ndi azibambo sapatsa ulemu kwenikweni mkazi amene akutengako mbali ku nkhani ya ndale. Pofuna kugonjetsa mzimai, azimuna ambili amagwilitsa nchito mau onyoza. Ambili amanena azimai amene atengako mbali m'ndale kuti ndi mahule kapena acimasomaso. Ena amanena azimai otele kuti ndi opanda mwambo. Simwinga (2006) anapatsa zitsanzo za mau amene azibambo ambili amagwilitsa nchito ponena mkazi amene amatenga mbali m'ndale. Iye ananena kuti mkazi amene amatengako mbali m'ndale amaitanidwa kuti hule, osakwatiwa bwino kapena opanda mwambo. Cifukwa cogwilitsa nchito mau otele, azimai ambili samatengako mbali m'ndale kotelo kuti ufulu weniweni woti iwo atengeko mbali kupanga malamulo ndi wocepa. Mau otele amabweza kumbuyo citukuko ca dziko. Miti (2008), ananena kuti munthu aliyense ali ndi ufulu wokamba zakukhosi kwake ndipo munthu amene alibe ufulu wokamba zakukhosi kwake sapeza cisangalalo pa ufulu wina uliwonse. Kucepa kwa azimai kumapezekanso pamalo anchito.

KUSIYANA KWA UFULU WA NCHITO MU ZAMBIA

Azimai ndi azibambo mdziko la Zambia amagwila nchito zosiyanasiyana. Monga madela ena onse padziko lapansi, azimai ndi atsikana ambili mu Zambia ndiwo amene amasunga ana ndi kufuna cakudya pa nyumba. Kagwilidwe ka nchito pakati pa azimai ndi azibambo kamasiyana malinga ndi malo amene anthuwa amakhala. Azimai ndi azibanbo ena amakhala mmidzi ndipo nchito zimene amagwila zimalingana ndizofunikila za malo amenewo. Gulu lina la azimai ndi azibambo limapezeka mu matauni ndipo nchito zimene anthuwa amagwila zimalingana ndi zofunikila za malowo. Ngakhale kuti pali kusiyana pa mtundu wanchito pakati pa anthu okhala m'matauni ndi mmidzi, kusiyana kwenikweni pakati pa azimai ndi azibambo kumapezeka pa kagawidwe ndi kagwilidwe kanchito.

Kusiyana kwa Ufulu Wanchito

Azimai ndi azibambo mu Zambia ali ndi ufulu wosiyana ndipo amagwilanso nchito zosiyana. Gawo ili la pepala lidzayesa kulongosola zakusiyana kumene kulipo pakati pa azimai ndi azibambo ndiponso pakati pa atsikana ndi anyamata, pakagwilidwe ka nchito mmanyumba ndi malo ena. Lidzayesanso kunena pa mavuto amene magulu amenewa amapezana nawo ndiponso kusiyana kumene kulipo pa nkhani makamaka ya ufulu wacibadwidwe pakati pao.

Kulingana ndi mitundu ya anthu ambili mu Zambia, mai ndiye amene amafunika kusunga nyumba. Kutanthauza kuti amafunika kusesa pakhomo, kusunga ana, kuona kuti zonse zofunikila pakhomo zilipo (Miti 2002). Ngati panyumba pali atsikana, mai amafunika kuphunzitsa anawo mkhalidwe wabwino kulingana ndi mwambo wa makolo awo. Mai amafunikanso kuphunzitsa ana kugwila nchito zomwe zimadziwika kuti ndi zacikazi. Mwana wamkazi amafunika kudziwa nchito monga kutsuka mbale, kusesa pakhomo, kucapa zovala zake ndi za abale ake, kuphika cakudya ndi kusunga ana anzake adakali wamng'ono. Mmalo ena monga mmidzi, mwana wamkazi amaphunzila kudzuka mmamawa kukatunga madzi ogwilitsa nchito panyumba. Amaphunzitsidwa kukhala ofatsa, odzicepetsa ndipo waulemu cifukwa cakuti ndi mkazi. Mwana mwamuna nayenso aphunzitsidwa kuti amafunika kukhala olimba mtima, wamphamvu ndipo amayenela kugwila nchito monga zotema nkhuni, kulima madimba ndi kumanga nyumba, nkhokwe ndi zina zotelo. Maphunzilo amenewa ndi ciyambi cosonyeza sankho pakati pa atsikana ndi anyamata kotelo kuti akakula ndi kutha msinkhu, atsikana amakhulupilila kuti iwo sangagwile nchito za anyamata ndipo anyamata naonso amakhulupilila kuti ali ndi mphamvu kupambana atsikana ndipo sangagwile nchito zacikazi. Mwacitsanzo, mwana mwamuna amauzidwa kuti '*ndiwe mwamuna osacita ngati wamkazi kulila lila*'. Ici cimatanthauza kuti kulila ndi kwa mwana mkazi osati mwamuna. Kulingana ndi makambidwe otelewa, mwana mwamuna amafunika kukhala olimba mtima ndipo misozi yake siifunika kuoneka kwa anthu. Citsanzo colingana ndi ici cinapatsidwa ndi Mhute (2008) amene ananena kuti mu ciShona ana amuna amawauza kuti asamacite zinthu ngati ana akazi. Cifukwa ca kakambidwe kotele ana amuna amayamba kuyankhula ndi udindo adakali ndi zaka zocepa. Iwo amakula ndi mtima wacikhulupililo pa nchito zao. Ana akazi amakula ndi mantha ndipo wopanda cikhulupililo pa nchito zao.

Nthawi zina, Makolo ndiwo amadzetsa sankho pakati pa ana akazi ndi amuna cifukwa ca kakambidwe kawo. Iwo amakonda kugwilitsa nchito mau onena kuti *"osakonda kupezeka ku cipinda cophikilamo cakudwa ndiwe mnyamata."* Mau amenewa nthawi zina amadzetsa vuto pa umoyo wa ana amuna cifukwa amacoka panyumba yamakolo awo osadziwa kuphika kapena kucapa. Cifukwa caici nthawi ikakwana yoti iwo ayambe umoyo wodzikhalila okha amakwatila msanga cifukwa anazolowela akazi kuwacitila nchito zimenezi. Cifukwa caici ena amaona akazi awo ngati anchito osati mthandizi wao. Pothela pake amacita nkhanza ndi kumanzunza mkazi waoyo. Ici cimakhala cinthu covuta kwambili mu umoyo wa mwana wamkazi cifukwa iye amauzidwa kuti afunika kusunga cikwati cake. Posadziwa kuti ali ndi ufulu wacibadwidwe iye amanzuzidwa nakhala cete kuti cikwati cake cisathe.

Mwana wamkazi amabweletsa cikondwelelo kwa makolo ngati ali ndi mkhalidwe wabwino ndipo amagwila bwino nchito panyumba. Zikatelo bambo amati mwana wanga ndi wanchito ndipo waulemu. Koma ngati mwanayo wacita cinthu coipa kapena watenga mimba, amakhala mwana wake yekha mkazi, ndipo bambo amati *"cimwana cako catimvetsa manyazi. Sunaciphunzitse mkhalidwe wa bwino."* Ena azibambo amapilikitsa akazi awo apanyumba pamene sanacite coipa ciliconse. Mkhalidwe wotele umacitika cifukwa azibambo ena amaganiza kuti mkazi wao ali ngati cimodzi mwazinthu kapena katundu amene iwo ali nawo. Conco mzimai amasowa ufulu wokamba zakukhosi napitiliza kukhala wopondelezedwa pa nyumba pake cifukwa ca miyambo ina yamakolo ndi maphunzilo enanso amene amapitamo akamakonzekela zakasungidwe ka nyumba mcikwati. Mkhalidwe wotelo ukupezekabe mmadela ena mu Zambia. Mmalo moti azibambo azisunga mabanja awo azimai ndiwo amasunga mabanja ndikufuna zofunikila zambili zapanyumba monga kulima cakudya.

Azimai ndiwo amalima cakudya cambili mmidzi yao. Azimai ambili mu Zambia amagwila nchito maola okwanila khumi ndi awili (maola 12) kusiyana ndi azibambo amene amagwila nchito maola cabe okwanila asanu ndi awili (maola 7) pa nchito ya ulimi. Ngakhale kuti azimai amagwila nchito maola ambili tele, malipilo awo amakhala ocepa kwambili. Nthawi yokolola mbeu zawo za mmunda, azibambo ena ndiwo amakhala patsogolo kutenga mbeu zija kukagulitsa. Pothela pake, iwo azibambo amatenga ndalama zambili napatsa akazi awo ndalama zocepa. Enanso amapanga ndondomeko ya zinthu zofunikila koma osafunsa akazi awo. Mkhalidwe umenewu umacitika kwambili mmidzi cifukwa ca mwambo wa

makolo wonena kuti mkazi amafunika kusunga malamulo a mwamuna wace ngati afuna kusunga cikwati cake. Mwambo umenewu umapondeleza azimai kuti asakhale ndi ufulu wokamba ndiponso kukhala ndi zinthu zao zao monga azibambo.

Ngakhale azibambo salima maola ambili, monga azimai, iwo ndiwo ali ndikatundu wambili. Alinso ndi ziweto ndi zida zolimila zambili. Azimai amakhala wopondelezedwa ndipo amapitiliza kukhala osauka. Zonsezi ndi zinthu zimene zimasowetsa mpata woti mwana wamakazi aphunzile. Popeza ndalama zimakhala zopelewela, azimai amauza ana akazi kuti adziwathandiza kugwila nchito kuti apeze cakudya cokwanila pa panyumba. Vuto limeneli limapititsa patsogolo kusadziwa kulemba ndi kuwelenga pakati pa ana akazi ndi kutinso adzikwatiwa adakali ndi zaka zocepa. Nawonso ana amenewa amapitiliza ndi mkhalidwe wamakolo awo wopondelezedwa ndipo wosowa ufulu wokhala ndi zithu zaozao. Ana amuna amapitiliza ndi maphunzilo awo kenaka kupeza nchito zabwino. Makolo amaiwala kuti kuphunzitsa mwana mkazi ndi kuphunzitsa dziko lonse cifukwa anthu amene amadzapeza phindu akaphunzila munthu wamkazi ndi ambili.

Kusowa mpata wopita kusukulu pakati pa azimai and atsikana m'madela ena makamaka mmidzi mdziko la Zambia, kumabweza kumbuyo unyinji wa zokolola zao mminda. Cifukwa cosadziwa kuwelenga ndi kugwilitsa nchito zitsulo monga makompyuta, iwo amapitilizabe kugwilitsa nchito njila zakalimidwe zakale zimene siziwaphindulila. Sadziwa njila zaulimi zatsopano, sadziwanso malonda amene iwo angatengeko mbali ndiponso mabanki amene amabweleketsa alimi ang'ono ang'ono ndalama zoti nkupititsa ulimi wawo patsogolo. Mwacitsanzo mu Zambia banki lochedwa *Zambia National Comercial Bank* (ZANACO) imathandiza alimi ang'ono ang'ono ndi ngongole kuti apititse patsogolo ulimi wao. Azimai amene sadziwa kuwelenga ndi kulemba amakhala ovutika ndipo umphawi kupita patsogolo. Cifukwa cosadziwa kuti ali ndi ufulu wopita kusukulu, umoyo wao umakhala wovutika ndipo wa umphawi kotelo kuti matenda monga a kaliondeonde amapitanso patsogolo.

UFULU PA MATENDA A KALIONDEONDE (EDZI)

Matenda a Kaliondeonde (Edzi) ndi matenda amene atsiliza anthu mmaiko ambili mu *Africa*. Matenda amenewa amakhuza kwambili maiko amene ali

kumwela kwa Africa. Anthu mazana ndi mazana akufa cifukwa codwala matenda amenewa. Anthu a mdziko la Zambia ndi amodzi mwa anthu amene akukhuzidwa ndi matendawa. Azimai ndi azibambo, atsikana ndi anyamata ndiponso ana akhanda naonso akukhuzidwa ndi matenda amenewa. Ngakhale kuti mbili ya matendawa inafalitsidwa mmadela ambili a mdzikoli, kuculuka kwa anthu amene ali ndi kacilombo ka matenda a kaliondeonde kuli kupitabe pastogolo. Malinga ndi cifufuzo cinacitika mcaka ca 2012 mu Zambia, anthu opitilila mmodzi pa anthu Seven ali ndi matenda a kaliondeonde. Gulu la azimai ndi limodzi mwamagulu okhuzidwa ndi matendawa. Malingana ndi kufufuza kunacitika mcaka ca 2012 mu Zambia, nambala ya azimai ndi atsikana azaka zobadwa pakati pa 15 ndi 24 odwala matenda a kaliondeonde limapambana nambala ya azibambo ndi anyamata odwala matenda amenewa (Zambia Statistics, 2012). Cimodzi mwazinthu zina zimene zimapangitsa kusiyana kwa nambalaku ndi vuto losowa ufulu wokamba pazinthu zimene iwo sanakondwele nazo. Ndiponso nthawi zina azimai amasowa mphamvu ndi ufulu wolankhula ndi azimuna awo kuti agwilitse nchito mphila (makondomu) pamene iwo sanakhutile ndi mayendedwe a azimuna ao. Ici cimasonyeza kuti azimai alibe mpata ndi mtendele kapena ufulu weni weni woti iwo nkudziteteza ku matenda amenewa. Azimai ndi amene amapezeka ndi matendawa kupambana azibambo cifukwa cakuti bungwe la likulu loyanganila pa za umoyo wa anthu mu Zambia linakhazikitsa lamulo lonena kuti mai aliyense amene ali ndi mimba amafunika kupimitsa kuti adziwe ngati alinako kacilombo ka Edzi kuti adziwe mmene mai ndi mwana angathandizikile nthawi yobeleka itafika. Lamulo limeneli linakhazikizidwa pofuna kucepetsa infa pakati pa azimai kapena ana akhanda pa nthawi yobeleka ngati ali ndi kacilombo ka Edzi. Ncifukwa cake nthawi zina nambala ya azimai odwala matenda a Edzi imapitilila nambala ya azimuna. Popeza nambala ya atsikana ndi azimai odwala matenda a Edzi imapitilila nambala ya anyamata ndi azibambo ndiponso popeza azimai ambili ndiwo amagwila nchito za ulimi, njala ndi umphawi zimapitililanso patsogolo.

Azimai amakhuzidwa kwambili ndi matenda a Edzi cifukwa ndi amene amasunga ana ndi nyumba. Ngati iwo adwala umoyo wa ana umakhala wosautsa kwambili. Nchifukwa cake pakati pa azimai ndi azibambo, azimai ndiwo amayesetsa kuyankhula ndi ana awo pa ubwino wozisunga ngati afuna kuti akhale ndi umoyo wautali. Amakhazika ana awo pansi ndi kuwaphunzitsa mmene anthu amatengela matendawa. Iwo amazindikila

kuti ali ndi danga loyankhula ndi kuphunzitsa ana awo pa zoipa zimene zimapezeka ngati munthu wadwala matenda akaliondeonde. Nthawi zambili azimai ndiwonso amene amayamba kukambilana ndi azimuna awo pa nkhani ya matenda akaliondeonde pofuna kuwacenjeza okondedwa awo zamavuto amene matendawa amabweletsa pa nyumba. Ufulu wolankhula pamatenda amenewa ulipo pakati pa azimai ambili. Ndipo ngakhale azibambo nawonso alinawo ufulu umenewu ambili mwaiwo samalankhula ndi azikazi awo nkhani yokhuza matenda a Edzi ngakhale kuti ndiyofunikila kwambili mmabanja mwawo. Kusaonetsa utsogoleli umenewu pakati pa azibambo pa matenda a kaliondeonde kumabweletsa kubisana ngati mmodzi mwaiwo apezeka wodwala. Cifukwa ca mkhalidwe wotele azimai okwanila asanu odwala matenda amenewa anafunsidwa kuti afotokoze mmene iwo anadziwila kuti ali ndi matenda akaliondeonde. Awili mwa azimai amenewa ananena kuti sadziwa ndipo enanso awili ananena motele:

1. Amuna anga ndiwo anandibweletsela matendawa. Iwo sanandidziwitse kuti ali ndi kacilombo ka Edzi. Pamene ine ndinapezedwa ndi kacilomboka iwo sanaoneke kudabwa ndipo anaulula kuti nawonso anali wodwala.
2. Ine sindinadziwe kuti amuna anga ali ndi kacilombo ka Edzi. Ine ndinadziwa zakudwala kumeneku pamene ndinakhala ndi mimba kuti ndili ndi matenda akaliondeonde. Amuna anga sanandiuze ndinadziwila kucipatala.

Mai wina ananena kuti:

> Amuna anga ndiwo anali pastogolo ndi nkhani yopimitsa cifukwa anadwala kwa ka nthawi.

Cifukwa ca mantha onena za matenda a Edzi pakati pa azimai ndi azibambo kupititsa patsogolo matenda amenewa azimai ambili amadziwa zakudwala kwa amuna awo pamene matenda apita kale pastogolo. Ena samadziwa mpang'ono ponse mpaka imfa ya azimuna awo. Azimai ambili mu Zambia amadzipeleka kusunga azimuna awo ngakhale akudziwa zamatenda awo. Samataya mtima koma amayesa yesa kuwasamalila mpaka imfa. Koma azimuna ambili sasamalila azikazi awo ngati apezeka ndi matenda akaliondeonde. Ena mwaiwo amapilikitsa azikazi awo komanso

ena samafuna kudziwa ngati ali nako kacilombo ka matenda akaliondeonde kapena ai. Azimai ambili nawonso samaulula ngati iwo ndiwo ayambilila kupezeka ndi matenda amenewa. Ufulu weniweni woti azimai azicingilize kumatenda akaliondeonde mmabanja palibe cifukwa ambili mwaiwo amawopa ngakhale kuuza azimuna awo kugwilitsa nchito makondomu ngati adziwa kuti azimuna awo ali ndi tusumbali. Ambili mwa azimai amafela mkati cifukwa cofuna kusunga cikwati cao. Izi zimacitika pakati pa azimai ambili mmadela osiyanasiyana mdziko la Zambia. Pofuna kuthesa vutoli, zipatala zaboma zambili mu Zambia zilimbikitsa kunena kuti mzimai amene ali ndi pakati afunika kupimitsa matenda a Edzi pamodzi ndi mwamuna wake. Ici cimathandiza akwati kudziwa za umoyo wao pamodzi. Mfundo imeneyi yathandiza kulimbitsa mabanja ndi kucepetsa kupasuka kwa mabanja cifukwa anansi kuzipatala amapeleka malangizo a mmene anthuwa amayenela kuzisunga ngati iwo apezeka ndi matenda amenewa.

Kusowa ufulu pakati pa azimai pa nkhani yokhudza umoyo wao, kuli kucepa pang'ono pang'ono cifukwa nkhani yokhudza matenda a Edzi yafalitsidwa mmadela ambili mu njila zosiyanasiyana. Ngakhale ndi mmasukulu momwe anyamata ndi atsikana akuphunzila pa zaufulu wolankhula ndikudziwa za umoyo wao pa nkhani ya matenda a Edzi.

MWAMBO NDI MAU OBWELETSA SANKHO MMASUKULU

Masiku akumbuyoku, mwana wamkazi sanali kuvomelezedwa kupita kusukulu. Anali kuuzidwa kuti abisale ngati olemba maina a ana apita mmanyumba kulemba maina. Ncifukwa cake zaka zakumbuyo nambala ya ana akazi amene anali kupita kusukulu inali yocepa. Ngakhale masiku ano, makolo ena savomeleza kuti ana awo kupita patsogolo ndi maphunzilo. Mwana wamkazi akatha msinkhu makolo ena akwatilitsa mwanayo kuti apezeko ndalama kapena cifukwa coopa kuti mwana wawo akapitiliza kupita kusukulu iwo sadzapeza phindu liliyonse cifukwa azafunika kumulipilila kusukulu. Nthawi zinanso ngati panyumba pali mwana wamkazi ndi wammuna, mwana wamkazi sapatsidwa ufulu ndi nthawi yokwanila kuti awelenge cifukwa amafunika kuthandiza kapena kugwila nchito zomwe zinapasidwa kwa iye. Kulingana ndi mwambo wa makolo, Mwana wamkazi ayenela kukhala ofatsa. Sayenela kukambakamba. Cifukwa ca mwambo wotele, ana akazi amakula osadziwa kuti ali ndi ufulu

wopita kusukulu. Nthawi zina anyamata amanena mau onyoza, koma cifukwa ca mwambo, iwo amakhala cete kuopa kuti angawaone ngati opanda ulemu. Aphunzitsi ena nawonso amasula zolankhula zimene anyamata amanena pofuna kupondeleza atsikana. Iwonso amatsata mwambo wonena kuti mwana wamwamuna amafuninka kukhala olimba ndipo opanda cibwana ndi mwana wamkazi ngati akufuna kuti apatsidwe ulemu. Cifukwa ca mwambo umenewu, ana ena akazi amakhala osamasuka kutengako mbali ngati aphunzitsi aphunzitsa mukalasi.

Ana amuna nawonso amasowa ufulu pasukulu ngati sacita bwino. Aphunzitsi amawakalipila anyamata pamaso pa atsikana nawauza kuti "*ndiwe mwamuna ufunika kuikapo nzelu pasukulu ngati ufuna ukakhale bwino mtsogolo.*" Mau amenewa amabweletsa sankho ndi kucotsa ufulu wopita patsogolo ndi maphunzilo pakati pa atsikana ndi anyamata. Ici cimaonetsa kuti mwana wamkazi safunika kukhala bwino, ndipo sukulu ilibe phindu kwa iye. Ncifukwa cake atsikana ambili saikako nzelu ku maphunzilo monga masamu ndi sayansi. Iwo amaona kuti maphunzilo amenewa ndi okhalila anyamata kotelo kuti ngakhale mwai wogwila nchito zimene anyamata amagwila ali nawo, iwo posaika nzelu ku phunzila maphunzilo amenewa, amadzimana mwai iwo wokha wogwila nchito za pamwamba.

Mkhalidwe uwu umapititsa pastogolo kucepa kwa ana akazi amene amafuna kupikisana ndi anyamata makamaka mumaphunzilo monga masamu ndi sayansi. Ngakhale atsikana ena ali ndi nzelu kupambana anyamata, iwo amapewa maphunzilo amenewa cifukwa camaganizo onena kuti maphunzilowa ndi a amuna. Mwacitsanzo pa sukulu yayikulu ya mu Zambia yochedwa *University of Zambia*, atsikana ocepa kwambili ndi amene amalowa mu sukulu ya *Natural Sciences* kuphunzila za ukatswili wazitsulo zosiyanasiyana kapena za udokotala. Zonsezi zimacitika cifukwa cosathandiza atsikana kukhala ndi cidwi mumaphunzilo amenewa. Atsikana amene amakwanitsa kupita patsogolo ndi maphunzilo samafuna kutengako mbali kuphunzila maphunzilo amene amadziwika kuti ndi acimuna. Ncifukwa cake ambili mwaiwo amagwila nchito zimene zimadziwika kuti ndi za cikazi. Nchito zimenezi ndi nchito monga za unasi, uphunzitsi ndi ulembi.

Kusiyana kwa ufulu pakati pa ana amuna ndi ana akazi pa nkhani ya maphunzilo kumacitikanso mmabanja. Pa banja pamene pali mwana wamkazi ndi wammuna, mwana wammuna samapatsidwa nchito ili yonse akakomboka kusukulu. Iye ali ndi ufulu wopitiliza kuwelenga kapena kukasewela ndi anzake. Koma mwana wamkazi alibe ufulu wotele popeza

iye ayenela kugwila nchito zimene zinapatsidwa kwa iye ngati mwana wamkazi. Amafunika kutsuka mbale, kusesa pakhomo, kuphika ndi nchito zina zotele (Simango 2002). Ici cimatanthauza kuti ngati anawa apatsidwa nchito kusukulu yoti akalembele kunyumba, mwana wamkazi sadzakhala ndi nthawi yokwanila kucita nchitoyi. Conco mwana wammuna amakhala ndi nthawi yaikulu yoti iye alembe nchito imene wapatsidwa. Kusiyanitsa kwa kasungidwe ka mwana wamkazi ndi wammuna nakonso kumalepheletsa mwana wamkazi pa sukulu. Cifukwa cosowa ufulu wolankhula pakusiyanaku, ana akazi ambili amalephela mayeso. Vuto limeneli limapititsa pasogolo umphawi mu umoyo wa anawa ndipo kumabweletsa sankho pakati pa ana akazi ndi ana amuna pakasankhidwe ka nchito. Ngakhale kuti nthawi zina ana ena acikazi amapeza mavuto otele, ena mwaiwo saikako nzelu kuzokamba za anthu, iwo amaika nzelu kumaphunzilo awo napambana mayeso ndi kupita ku ma koleji kapena ku masukulu apamwamba a ku yunivesiti.

Atsikana nthawi zina amapeza vuto lasakho kucokela ku ana asukulu anzao makamaka anzao anyamata. Izi zimacika ngati mwana wacikazi apambana anzake onse mu kalasi. Ana acimuna amafunafuna mlandu woti acotse ufulu ndi mtendele wa mwana wacikazi pomagwilitsa nchito mau onena kuti wagwilitsa nchito thupi lake kuti azipatsidwa ma malikisi abwino. Izi zimanenedwa pofunitsitsa kuonetsa kuti mwana wamkazi sangapambane mwana wammuna. Mau amenewa amacotsa ufulu womwe mwana wamkazi afunika kukhala nawo pa sukulu. Ana akazi ena naonso samafuna kulimbitsa mzawo pamene mau onyoza otele akukambidwa. Iwonso kambilimbili amathandiza anyamata kulankhula zinthu zosayenela pa mzawo. Ncifukwa cake cidani sicitha pakati pa azimai cifukwa cosagwilizana.

Kusowa ufulu ndi mtendele pakati pa atsikana mmasukulu apamwamba kumapezekanso mu timabungwe totsogolela anzao. Anyamata ambili ndi amene amapatsidwa mpata wotsogolela anzawo. Atsikana amene amaimilila anzao ndi ocepa kwambili cifukwa ana asukulu ambili mmasukulumu ndi amuna ndipo iwo sakhulupilila kuti mstikana angakwanitse kuwaimilila pa nthawi ya mavuto. Masiku akumbuyoku azibambo ambili ndiwo anali kulamulila ndi kutsogolela masukulu ambili. Koma masiku ano zinthu zili kusintha pang'ono pang'ono cifukwa azimai nawonso alikupatsidwa udindo wotsogolela anzao mzinchito zosiyanasiyana mu Zambia.

SANKHO PA NCHITO

Vuto losowa ufulu silikhudza atsikana okha mmasukulu komanso azimai mmalo anchito. Azimai amafunika kukhala odzicepetsa pa nchito kulingana ndi mwambo wacikuda. Ncifukwa cake azimai ambili amagwila nchito za pansi monga za ukalaliki ndi ukalemba pamene azibambo amapatsidwa nchito za pamwamba zimene zimawathandiza kupita patsogolo ndi maphuzilo ndiponso kupatsidwa udindo wotsogolela. Ngakhale kuti masiku ano azimai ena nawonso akupatsidwa udindowu, ciwelengelo cawo ndi cocepa kwambili. Mwacitsanzo mdziko la Zambia, simunakhaleko mtsogoleli (pulezidenti) wamkazi kucokela nthawi imene Zambia inatengela ufulu mcaka ca 1964. Monga momwe Katebe (2014) analemba mupepala lonena pa za azimai amene anasankhidwa kukhala a phungu mnyumba ya malamulo pa 12 September, 2014, azimai okwanila 20 cabe pa anthu 158 ndi aphungu mnyumba ya malamulo mdziko la Zambia. Ici cimatanthauza kuti aphungu 138 mnyumba ya malamulo ndi azibambo.

Cinanso ndicakuti makampani ambili akuluakulu, monga mabanki, maunivesiti, atsogoleli ambili ndi azibambo. Mwacitsanzo, kucokela mmene *University of Zambia,* inakhazikizidwa, mcaka ca 1966, kulibe mai ndi mmodzi yemwe amene anapatsidwa udindo wotsogolela sukuluyi. Azimai okwanila awili cabe ndiwo anapatsidwa mwai wokhala atsogoleli aciwili pa sukuluyi. Cinanso ndi cakuti aphunzitsi akazi pa sukuluyi ndi wocepa kwambili. Azibambo ambili mdziko la Zambia ndi amene amatsogolela masukulu a masekondale ndi mapulaimale ngakhale kuti azimai ndiwo ambili mdziko. Azimai ambili amene ali paudindo sapatsidwa ulemu kwenikweni ndi anchito ena amuna. Amuna ena amataya ulemu mmakambidwe awo cifukwa safuna kutsogololedwa ndi mkazi.

Nthawi zina, munthu wamkazi angafike pa nthawi yoti iye nkupatsidwa udindo wa pamwamba koma cifukwa cakuti wakhala ndi mimba, undindo uja umapatsidwa kwa munthu wina. Azibambo ndi amene amakhala ndi mwai wopatsidwa udindo umenewu ngakhale kuti nthawi zina iwo ali ndi maphunzilo osakwanila. Sankho lotele limabweletsa citukuko ca dziko kumbuyo. Mkazi safunika kulandidwa mwai wotsogolela cifukwa cakuti ali ndi mimba. Kukhala ndi mimba sicifunika kukhala cilango colanda mkazi ufulu woti iye nkupatsidwa udindo. Azimai, monga azibambo, nawonso ali ndi ufulu wopatsidwa udindo ngati iwo ali ndi maphunzilo ndi mapepala oyenela. Nthawi zina azimai amapita mmayeso osiyanasiyana pofuna

nchito. Ena samapatsidwa nchito ngakhale kuti ali ndi mapepala ofunikila ngati akana kucita zadama ndi wolemba nchito pa nchitopo. Ena samakhala ndi mwai wopatsidwa nchito ngati maonekedwe awo ndi osakoka mtima azibambo. Ngakhale azimai ena ndi osakongola nkhope, ali ndi luso ndiponso nzelu zoti iwo nkutsogolela anzao bwino. Olemba nchito amaiwala kuti mulungu samana zonse. Ncifukwa cake aCewa amati *'ukaipa dziwa nyimbo'*: kutanthauza kuti ngati munthu ulibe maonekedwe abwino ufunika kudziwako cinthu cimodzi cimene anthu angakhumbile mu umoyo wako.

Nthawi zina miyambo nayonso imabweletsa mavuto pakati pa azimai pa nchito. Kucokela kale lomwe, azimai ali ndi nchito zawo ndipo azibambo nawonso ali ndi zinchito zawo. Azimai ambili amene sanapite patsogolo ndi maphunzilo ndi amene amagwila nchito zamalonda. Iwo amakonda kugulitsa malonda awo mmisika. Mmatauni ndi mmidzi mowe misika imeniyi imapezeka. Ndipo malonda amene azimai amakonda kugulitsa ndi malonda monga ndiwo zamasamba, cimate ndi thelele. Amagulitsanso kapenta, nsomba zouma, nzimbe, nthoci, ndi zina zace. Azimai amene anatukuka pa nchito za malonda amagulitsanso zinthu monga mbatatisi ndi mpunga. Ngakhale nchito zogulitsa pamsika zimadziwika kuti ndi za azimai, masiku ano azibambo nawonso amapezekapo. Ici cimatanthauza kuti azibambo ali ndi njila zambili zimene iwo amapezela ndalama kusiyana ndi azimai. Azibambo amene amapezeka pa msika pamodzi ndi azimai amalandilidwa popanda vuto namacitila malonda pamodzi ndi azimai. Apa tikuona kuti azibambo ali ndi ufulu wogwila nchito mmalo osiyanasiyana kopanda vuto. Koma azimai sangapezeke mmalo onse anchito mmene mumapezeka azibambo monga mmalo omanga manyumba ndi kukumba miyala pa migodi. Nchito yomanga nyumba ndi nchito imene imadziwika kuti ndiyovuta. Kotelo kuti azimai ambili satengako mbali.

Nchito yokumba miyala pamigodi ndi ina mwa nchito zimene zimadziwika kuti ndi za cimuna. Azimai sagwilako nchito zimenezi cifukwa ca kulimba kwa nchito zake. Nchito zina monga kukonza magalimoto ndi udokotala nazonso zinali kudziwika kuti ndi nchito za amuna. Popeza masiku ano azimai nawonso akugwilako nchito zimenezi, onena amafuna ndithu kuonetsa kuti ngakhale ndi nchito za azibambo koma azimai nawonso aliko amene amagwila nchitozo. Ncifukwa cake pofuna kuonetsa kusiyana onena amati makanika wamkazi kapena dokotala wamkazi cifukwa nchito zimenezi ndi nchito zimene zinali kugwilidwa ndi amuna

okhaokha kale dziko la Zambia likadali mwana. Cimodzimodzi, amuna amene amagwila nchito za unasi amaitanidwa kuti *anasi amuna* cifukwa nchito yosunga odwala ndi nchito imene inali kugwilidwa ndi azimai. Mau amene agwilitsidwa nchito ponena nchito zimene anthu akugwila nawonso amaonetsa sankho. Cifukwa ca sankho limeneli anthu ambili odwala akapita kucipatala samafuna kuonana ndi dokotala wamkazi. Kulingana ndi maganizo a anthu amenewa, dokotala wammuna ndiye dokotala weniweni amene amadziwa nchito.

Sankho pakati pa azimai ndi azibambo silipezeka pa nchito pokha komanso mmalo okhalamo ndi mmene anthu amagwilitsila mau mmakambidwe awo. Anthu pofuna kulankhula nkhani zina kapena kuweluza mlandu amagwilitsa nchito mau okuluwika amene amachedwa kuti miyambi. Miyambi imeneyi nthawi zina nayonso imadzetsa sankho pakati pa anthu.

MIYAMBI YODZETSA SANKHO

Monga tanenela mndime yostilizayi, miyambi ndi mau okuluwika imene imagwilitsidwa nchito pofuna kunena pacinthu, kuweluza mlandu kapena kupeleka phunzilo pa zinthu zosiyanasiyana. Kambilimbili, miyambi imagwilitsidwa nchito pofuna kuphunzitsa munthu yemwe walakwa kapena kuthetsa vuto pakati pa anthu. Nthawi zina imanenedwa pofuna kuonetsa kusiyana kumene kulipo pakati pa azimai ndi azibambo. Ngalande (2013) analemba zamiyambi yosiyanasiyana ndi mmene anthu amagwilitsila nchito miyambiyo. Popeza miyambi imagwilitsidwa nchito mnjila zambili, mu ndime iyi tidzayesa kupatsa zitsanzo za miyambi imene anthu amagwilitsa nchito pofuna kuonetsa sankho pakati pa azimai ndi azibambo mmalo okhalamo. Mwambi woyamba umene uwonetsa sankho umanena kuti:

3. Mwana wa mzako n'kasambe kumanja wako n'kazidya.

Mwambi uwu umagwilitsidwa nchito ponena za makhalidwe a azimai ena oipa mitima amene safuna kusunga kapena kusamala ana a anzawo koma iwo amakonda kusakha, amazikonda ndipo salingalila zosowa za anzao ena. Ndizoona kuti kuli azimai ena oipa mtima omwe samafuna kuthandiza kapena kusunga ana aanzao. Komanso kulinso azibambo oipa mitima omwe safuna kusunga ana amunthu wina. Koma kulibe mwambi

umene umanena za makhalidwe a umbombo pakati pa azibambo. Azibambo ena ndi aumbombo kwambili cifukwa iwo amamana ndi ana awo omwe. Iwo sasiya ndalama kapena zakudya zokwanila panyumba. Iwo akaona kuti panyumba pali thelele amapita kukagula cakudya cabwino nadya iwo wokha. Ngakhale kuti anthu akudziwa za umbombo wotele, iwo sanena kanthu pa umbombowu.

Anthu ambili amakonda kunene zoipa zomwe azimai amacita kusiya zoipa zimene azibambo amacita. Mwacitsanzo, azibambo ambili sasunga malonjezo awo apacikwati. Amalumbila kuti adzakonda mkazi wao mpaka imfa. Koma mkazi wao akali moyo ena mwaiwo amakwatila mkazi wina kapena kukhala ndicisumbali. Iwo amafuna kuti mkazi wao amvetsetse cifukwa cakuti iwo ndi amuna. Azimai ambili amafela mkati nasunga cinsinsi pofuna kusunga cikwati cao. Koma ngati mkazi ndiye amene wakhala ndicisumbali, cikwati cimatha mwamsangamsanga. Azimuna amapatsidwa mphamvu zocita zinthu zadama cifukwa mwambo umatelo popitila mu miyambi imene imafuna kuteteza mkhalidwe wao monga mwambi uli pansipa:

4. Cigololo ndi wamkazi.

Mwambi umenewu umatanthauza kuti mkazi ndiye ali ndi mphavu yoti cigololo cicitike. Ngati mkazi wakana, cigololo sicingacitike. Mwambi umenewu ungayelekezedwe ndi mwambi wa ciBemba umene umanena kuti *"ucende wa mwaume tautoba ing'anda"* kutanthauza kuti cigololo ca mwamuna sicipasula nyumba. Mwambi umenewu umapatsa mphamvu amuna kumacita zadama cifukwa iwo amadziwa kuti pamene cinsisi cao cadziwika mkazi ndiye adzasekedwa ngakhale kuti cigololo ndi anthu awili. Palibe mwamuna, mkazi sangacite zadama ndipo palibe mkazi mwamuna nayenso sangacite zadama. Molingana ndi mwambo wa anthu akuda, mwamuna ndiye amafuna mkazi. Koma molingana ndi mwambi umenewu ngati onse mkazi ndi mwamuna agwidwa ali kucita zadama, mbili yamkazi ndi imene imaulutsidwa kwambili. Onena amati, "*aujee anawagwila cigololo*", kuchula dzina la mkazi. Ndipo ngati mwamuna okwatila ndi mkazi okwatiwa agwidwa ali kucita zadama, mkazi amasekedwa ndi kunyozedwa kuposa mwamuna. Ambili azimai amapilikitsidwa mcikwati cifukwa cavuto limeneli. Koma mwamuna wokwatilayo akapempha cikhululukilo, cikwati cake sicitha ndi mkazi wake. Ikacitika nkhani yoteleyi azimai amakhululukila azimuna awo napitiliza kukhala bwino panyumba pawo.

Cifukwa ca miyambi yotele, azimuna amapatsidwa mphamvu zocita cigololo pozindikila kuti dzina la mkazi ndilo limene lidzaonongeke. Ncifukwa cake azimai ambili amakhala alibe ufulu ndi mtendele mu zikwati zao. Matenda akatengela naonso amapita patsogolo cifukwa ufulu weniweni woti azimai angathetse cikwati cawo cifukwa ca uciwelewele wa amuna awo ndi wocepa kwambili. Ambili amafela mkati pofuna kuteteza amuna awo. Mwambi wina wolingana ndi mwambi wa ciwiliwu ndi:

5. Anakazi ni matuvi a mbuzi.

Mwambi uwu ndi wa mu ciNsenga, cinenelo cimene cimapezeka ku dela la ku mmawa kwa dziko la Zambia ku boma la Chipata ndi Petauke. Mwambi umenewu umatanthauza kuti *"akazi ndi matuvi a mbuzi"*. Molingana ndi zimene analemba Ngalande (2013) pa nkani yokhudza miyambi, mwambi umenewu umayelekeza akazi ngati matuvi a mbuzi cifukwa matuvi amenewa ndi osiyana ndi matuvi a nyama zina monga ng'ombe ndi nkhumba cifukwa amakhala owulungana, otaikana ndipo ambili. Tanthauzo lenileni la mwambi uwu ndi lakuti akazi ndi ambili monga matuvi a mbuzi. Ngati mkazi umodzi wakana mwamuna kapena afuna kukula mutu mnyumba, mwamuna safunika kuvutika mumtima cifukwa aliko akazi ena ambili ndipo okongola kupambana yemweyo. Mwambiyu umagwilitsidwa nchito pofuna kulimbitsa amuna amene amakanidwa akafuna mkazi ndiponso amuna amene amafuna kupondelezedwa ndi akazi awo.

Mwambiwu umaphunzitsa amuna kukhala ndi mtima wodzitama ndipo wosasamala mmene akazi amamvela cifukwa iwo angafune mkazi aliyense ndipo angapilikitse mkazi wawo nthawi iliyonse ngati iye akukula mutu. Amuna amapeza cilimbikitso ca mtima mmwambiwu cifukwa iwo sangafe ndi mtima kapena kuda nkhawa cifukwa ca mkazi. Iwo amaona munthu wamkazi ngati cithu cimene iwo angataye ndi kudoba nthawi iliyonse. Cifukwa cakakambidwe kotele, akazi ambili amakhala ngati akapolo opanda ufulu mzikwati zawo poopa kuti amuna awo angawaleke ndi kukwatila mkazi wina. Mwambi winanso mu ciNsenga umene umanena za makhalidwe ndi ufulu wa azimai ndi azibambo ndi:

6. Ucende ni matuvi opoza kutali.

Mwambi uwu umatanthauza kuti *"ucende ndi matuvi oponya kutali"*. Ngalande (2013) ananena kuti ucende umayelekezedwa ndi matuvi cifukwa cakuti matuvi sicinthu cabwino kucipenya kapena kukhala naco pafupi. Anthu kalelo amapita kuchile lakutali kukazithandiza kapena amakumba zimbudzi. Nthawi zino manyumba ambili ali ndi zimbudzi zamadzi zimene sizimasunga dothili. Mwambi umenewu umatanthauza kuti ucende sicithu cabwino. Kulibe mkazi kapena mwamuna amene angakondwele ngati okondedwa wake wagwidwa ali kucita ucende. Ucende uli ngati cinthu conyansa kucipenya ndipo anthu atsimikiza kuipa kwake. Ngakhale zili tele mwambiwu umabvomeleza amuna kucita ucenda malinga ngati acitila kutali kumene mkazi wao sangadziwe. Miyambi yonseyi siithandiza kubweletsa ufulu ndi mtendele mu umoyo wa azimai. Azimai amakhala onzunzika mu mtima ndipo amasowa ufulu mmanyumba ndi mzikwati zawo. Mwambiwu umagwilitsidwa nchito kwambili ngati mwamuna amakhala ndi zisumbali pafupi mosabisa konse. Masiku ano azibambo ena amagwilila ana a mnyumba mwao mwacikakamizo. Azimuna amene ali ndi mkhalidwe wotele amawaweluza pothilapo mwambi umenewu.

Azimai akadandaula pamakhalidwe a azimuna awo, oweluza amagwilitsa nchito mwambiwu. Zonsezi sizithandiza azimai. Azimai amakhala okwinya komanso cifukwa amafuna kusunga cikwati cao, amafela mkati. Azibambo amapatsidwa ufulu wocita zosayenela kupitila mu miyambi kotelo kuti ucende umavomelezedwa kwa azibambo osati kwa azimai. Cinanso miyambi nayonso imadzesa sankho pa makhalidwe pakati pa azimai ndi azibambo.

Ngakhale kalelo zinali tele, azimai ambili masiku ano acangamuka. Akadziwa kuti mwamuna wawo wayenda ngati *'fisi'*, iwo amamupilikitsa kapena kukampeleka kukhoti kuti cikwati cithe. Mwacitsanzo, masiku akumbuyoku, mu Zambia munali lamulo lonena kuti mkazi amene ayenda ndi mwamuna wamwini afunika kuzengedwa mlandu umene unali kuchedwa kuti *'marriage interferance* pa cingelezi kutanthauza kuti iye akusokoneza cikwati ca munthu wina. Masiku ano lamulo limeneli linacotsedwapo kutanthauza kuti azimai alibe citetezo cokwanila mzikwati zao. Mbali ina imene azimai ndi azibambo amapeza vuto ndi nchito ya umutekenya.

SANKHO PA NCHITO YA UMUTEKENYA

Kalelo azibambo ndi amene anali kugwila nchito ya umutekenya ndipo ndiwonso anali ndi magalimoto. Koma masiku ano azimai nawonso amagula ndikuyendetsa magalimoto awoawo. Anthu ambili pamene akufuna kugulitsa magalimoto omwe anali kuyendetsa amakonda kunena kuti galimotoyo inali kuyendetsedwa ndi mai pacingelezi amati *'lady driven vehicle'*. Nthawi zina mau amenewa ndi azoona koma nthawi zinanso mauwa agwilitsidwa nchito kuti galimotolo igulidwe mwamsanga. Mau amenewa amasonyeza kuti magalimoto amene amayendetsedwa ndi azimai amayendetsedwa mosamala. Ngakhale kuti ogulitsa magalimoto akuzindikila kuti azimai ambili amasamala kasungidwe kamagalimoto awo, mdziko la Zambia, amutekenya ambili makamaka aamuna amagwilitsa mau oipa pofuna kunena mmene azimai amadekhela mtima akamayendetsa magalimoto awo pamseu. Ambili amati; *'onani ndi mzimai amene ali kuyendetsa galimoto. Waiwala kuti ali pamseu. Iye akuona ngati ali kunyumba.'* Enanso amati, *onani ndi mkazi ali kusiteling'i. Waiwalako, akuona ngati akudya nsima!*

Zitsanzo zapatsidwa pamwambapa zikusonyeza kuti, azibambo ambili akali nawo maganizo onena kuti mzimai amafunika kupezeka panyumba osati kumayendetsa magalimoto pamseu. Ncifukwa cake amagwilitsa mau monga *'akuona ngati ali kunyumba'*. Cinanso tikaona mau otsatila omwe agwilitsidwa nchito mcitsanzo caciwili ndi *'kusiteling'i'*. Mau amenewa abwelekedwa mu cingelezi *(steering)* pofuna kuonetsa kuti kuyendetsa galimoto simalo a munthu wamkazi. Iye wabweleka cabe malowa cifukwa malo ake ndi kucipinda kophikila kapena kodyela nsima. Kulankhula kotele kumasonyeza sankho limene azibambo ambili akali nalo pa azimai. Iwo amaona kuti mzimai sangayendetse galimoto pamseu cifukwa iye amafunika kukhala kumbuyo kwagalimoto ndi kumasusunthila ana.

Sakho pakati pa azimai ndi azibambo limaonekanso ngati pamseu pacitika ngozi imene ikukhudza anthu awiliwa. Ngakhale kuti olakwa ndi bambo, iye amafuna kusambila mlandu mtekenya wamkazi. Amacita zimenezi pofuna kuonetsa kuti munthu wamkazi safunika kuyendetsa galimoto. Koma ngati ndi bambo wasokoneza pa museu, onena amati, ndi ngozi. Akazi amanenedwa kupambana amuna pa mseu. Izi zimacitika cifukwa cakuti amuna ambili samvetsetsa kuti azimai naonso ali ndi ufulu woyendetsa magalimoto pamsewu monga azibambo. Anthu ambili akali ndi maganizo onena kuti malo amuthu wamkazi ndi panyumba.

Ngakhale azimai ambili ndi amutekenya mu Zambia, amene amayendetsa magalimoto kapena mabasi amene amanyamula anthu ndi owelengeka kwambili. Masiku akumbuyoku, anthu ambili anali kuti akazindikila kuti mutekenya wabasi ndi mkazi, ena amatuluka mubasimo cifukwa cakuti analibe cikhulupililo mwa iye. Mdziko la Zambia azimai amene amayendetsa ma basi ndiwocepa kwambili. Ndipo akazi amenewa sayendetsa mabasi akuluakulu amene amanyamula anthu mmizinda yosiyanasiyana. Pamene ndinafunsa mtekenya wina wamkazi mmenene amapezela nchito yaumutekenya, iye anati:

> Nchito imeneyi siyapafupi ayi cifukwa anthu ambili alibe cikhulupililo mu mutekenya wamkazi. Kukhala mutekenya wamkazi, ufunika kukhala wolimba ndipo wosula zokamba za anthu.

Kucotsako nchito yoyendetsa mabasi, azimai ena amagwila nchito yoyendetsa matakisi. Awa ndi magalimoto amene amanyamula anthu kucoka pamalo amodzi kupita kumalo ena. Anthu ambili amene amayang'anila nchito yotele, amalemba nchito anthu amuna osati akazi. Akazi nawonso ambili safuna kugwila nchito imeneyi mu Zambia cifukwa cakuti iwo ndi azimai ndipo, m'malingana ndi mwambo wamakolo, malo awo ali pa nyumba osati pamsewu. Iwo amafunika kusunga nyumba zawo mwaudongo ndipo amafunika kuona kuti ana nawonso akusungidwa bwino. Pokhala mai wa panyumba, iwo amayenela kuona kuti cakudya cilipo cokwanila pakhomo kotelo kuti nchito zina monga zoyendetsa matakisi zimakhala zovuta kwa azimai. Cifukwa cakucepa kwa nambala ya azimai amene amayendetsa matakisi mu Zambia, azimai ndi azibambo oyendetsa magalimotowa anafunsidwa kunena zifukwa zimene zinapangitsa azimai ambili kusatengako mbali kunchito imeneyi. Mwacitsanzo mmodzi mwa amutekenya amuna ananena motele:

> Azimai safunika kugwila nchito imeneyi cifukwa ndi nchito yovuta. Nthawi zina timanyamula zigawenga kapena matsotsi ndipo mkazi sangakwanitse kugonjetsana nawo anthu amenewa. Ine pa ine ndekha sindingavomeleze mwana wanga wamkazi kapena mkazi wanga kukhala mutekenya wa matakisi.

Tikaonetsetsa mau amenewa, tiona kuti ngakhale anthu amanena kuti azimai ali ndi ufulu wocita zimene iwo akufuna, ufulu weniweni palibe

cifukwa cakuti azibambo ena ndi amene amasankha nchito zimene iwo akuganiza kuti akazi awo angacite. Iwo akali nawo maganizo osankha nchito zimene azimai awo afunika kugwila. Cinanso amutekenya ena pamene anafunsidwa maganizo awo pa ufulu wa azimai kuyendetsa matakisi, iwo anati:

> Muno mdziko lathu la Zambia zinthu zambili zasintha. Ine siningaletse mkazi wanga kukhala takisi dalaiva ngati iye afuna. Cacikulu ndi cakuti afunika kudziwa kuti iyi nchito siyapafupi ayi. Nthawi zina dzuwa limalowelamo osapangako ndi kakhobili komwe ayi. Nthawi zinanso timanyamula zigawenga. Ine ndingamumasulile kuti pokhala mkazi azimuna nthawi zina angafune kucita nawe zadama ndipo ufunika kulimba cifukwa azimai ambili amaphedwa ngati iwo akana kucita zadama ndi munthu amene iwo anyamula.

Mau monga amene anenedwa apa akusonyeza kuti, azibambo ena analandila uthenga wa ufulu wa azimai ndipo iwo alibe vuto kuvomeleza azimai awo kugwila nchito zimene zinali kudziwika kalelo kuti ndi zacimuna. Kwa iwo cofunikila kwambili ndi cakuti mzimai amene akufuna kugwila nchito monga yoyendetsa matakisi afunika kukhala olimba ndipo wachelu cifukwa zovuta za pa mseu ndi zambili. Tikaona mayankho a azibambo makumi awili amene anafunisidwa pa zimene iwo akuganiza pa nchito yoyendetsa matakisi azimai, tipeza kuti asanu ananena kuti iwo analibe vuto kuti azimai nkugwila nchito zimene zinali kudziwika kuti ndi za azibambo kale. Ndipo enanso khumi ndi asanu ananena kuti iwo sangavomeleze makamaka akazi awo kugwila nchito zotelezi cifukwa nchitozi ndi zovuta ndipo siziyenela azimai. Molingana ndi amuna ena, iwo amakhulupilila kuti azimai safunika kugwila nchito zolimba cifukwa ca mmene matupi awo anapangidwila. Kunena koteleku kumavomeleza zimene Aristotle ananena kuti Azimai ndi wofoka ndipo akakhala ndi mimba amapita mmavuto osiyanasiyana. Ena amamva cizunguzungu ndipo angacite ngozi pamseu.

Enanso ananena kuti nkhani zonena za ufulu wa azimai zabweletsa mavuto mu mabanja ambili. Azimai sapatsa ulemu azimuna awo ndipo mwambo wa anthu waonongeka. Iwo pofuna kuthandiza azikazi awo, amawayambitsa malonda ena amene angathandize kupeza ndalama mwaubwino kopanda ziopyezo monga zimene iwo anali kupitamo. Ici cikusonyeza kuti ngakhale uthenga unafalitsidwa wonena pa za ufulu wa

azimai, sianthu onse amene abvomelezana nawo uthenga umenewu cifukwa ena adakali kuona cifunilo coteteza mtundu wa azimai kumavuto ophedwa, kuvulazidwa kapena kugonedwa mwacikakamizo. Nchito ina imene azimai adakali ocepa ndi nchito yoyendetsa malole.

Magalimoto ena amene amanyamula katundu wamalonda ndi malole. Amutekenya ambili amene amayendetsa magalimotowa mu Zambia ndi azibambo. Azimai pa iwo wokha amaopa kuyendetsa magalimoto awa. Mantha amenewa ndi cifukwa cosiyanitsa kugawa kwa nchito pakati pa azimai ndi azibambo. Nchito yoyendetsa malole imadziwika kuti ndi nchito yovuta ndiponso yoopsa. Kudela lakumawa kwadziko la Zambia, muboma la Chipata, anthu amagwilitsa nchito njinga kunyamula anthu ndi katundu. Azimai ambili amadziwa kuchova njinga. Koma pakali pano azimai okwanila awili cabe ndiwo anagwapo kugwila nchito imeneyi.

Mmalo ena mu Zambia anthu amagwilitsa nchito ma wilibala kunyamula katundu wa anthu kupeleka kumalo komwe iwo atumidwa. Azimuna ndi amene amagwila nchito imeneyi. Azimai sagwilako nchito imeneyi cifukwa iwo amakhulupilila kuti nchito imeneyi imafunika anthu amphamvu. Ici cikusonyeza kuti sankho nthawi zina limacokela kwa iwo wokha azimai cifukwa camaganizo onena kuti mwamuna pokhala mutu mnyumba, iye amayenela kufuna ndalama pa nyumba. Nthawi zina azimai amasankha nchito zogwila cifukwa ca ciphale cosankha nchito zimene iwo amaona kuti angagwile. Ncifukwa cake azimuna ambili ndi amene amanyamula anthu pa njinga kuwapelaka kumalo osiyanasiyana ndipo amagwilitsanso nchito mawilibala kunyamula katundu kukapeleka kumalo kumene iwo atumidwa.

Mmalingana ndi mwambo wa anthu a mitundu yosiyanasiyana mu Zambia, amuna ndiwo amene amafunika kuyendetsa mabasi, matakisi kapena malole. Amuna ndiwonso amafunika kugwila nchito zocititsa thukuta monga kuchova njinga ndi kuyendetsa mawilibala. Azimai safunika kugwila nchito monga yoyendetsa malole, mabasi ndi matakisi cifukwa ca zovuta zimene zimapezeka mzinchito zimenezi. Oyendetsa mabasi akuluakulu mwacitsanzo, amaonekela panyumba patapita masiku angapo mmalinga ndi kumalo kumene iwo anatumidwa kukagwila nchito. Amutekenya amalole iwo amaoneka panyumba nthawi zina patapita mwezi–cinthu cimene mwambo subvomeleza munthu wamkazi kuti acite.

MAU OTSILIZA

Potsilizila, tiona kuti azimai ambili mu Zambia sadziwa za ufulu wao wacibadwidwe. Kusiyana kwa ufulu pakati pa azimai ndi azibambo kukalipo kwambili mmasukulu, pa zinchito ndi mmalo ena. Cinthu cimodzi cimene cimadzetsa kusiyana kwa ufulu pakati pa azimai ndi azibambo ndi mwambo wa makolo umene unagawa nchito zimene zimachedwa zacikazi ndi zimene zimachedwa zacimuna. Amuna ena savomela kutsogololedwa ndi azimai. Enanso amuna savomela kugwila nchito pamodzi ndi azimai mmagulu awo anchito, monga nchito ya umutekenya cifukwa iwo anatsimikiza kuti umutekenya simalo amene azimai amayenela kupezeka. Azimai amafunika kusunga nyumba zawo bwino osati kumakhala pa mseu.

Magulu a anthu nawonso anagawa nchito za azimai ndi nchito za azibambo. Cifukwa ca kugawa nchito kumeneku, azimai alibe ufulu weniweni woti iwo angagwile nchito zimene zimadziwika kuti ndi zacimuna. Nchito monga zoyendetsa mabasi, malole ndi matakisi zimadziwika kuti ndi nchito zacimuna. Makamaka nchito zocititsa thukuta monga kuchova njinga ndi kuyendetsa mawilibala ndi nchito zimene zimadziwika kuti ndi zacimuna. Mkazi amene amagwila nchito zotelezi amamuitana kuti ndi mwamuna. Cifukwa cakalankhulidwe ndi kagawidwe kanchito kameneka, azimai alibe mbali ku nchito monga zonyamula katundu pawilibala ndi panjinga.

Ciphale cimene azimai ali naco naconso cimacepetsa mwai woti azimai nkugwila nchito zimene azibambo amagwila. Ici cikutanthauza kuti mwai wogwila nchito zosiyanasiyana monga zimene azibambo amagwila ndi wocepa pakati pa azimai cifukwa ca ciphale, umbuli pa nkhani ya ufulu wacibadwidwe, mwambo wa makolo, sankho ndi cilengedwe ca munthu wamkazi. Azimai nawonso paiwo wokha, samvelana ndipo amacitilana kaduka kotelo kuti kugwilizana kwenikweni panchito kudakali kocepa. Malingana ndi zimene zinafufuzidwa, dziko la Zambia lingatukuke ngati azimai adziwa za ufulu wacibadwidwe umene iwo ali nawo. Akatelo, iwo adzakhala ndi mphamvu zolankhula ngati sanakondwele ndi zonena za anthu kapena malipilo pa nchito imene akugwila. Kupata ufulu kudzathandiza azimai kugwapo pa nchito zacitukuko ca dziko. Ici cikutanthauza kuti azimai adzatengako mbali kunchito zimene azibambo amagwila kotelo kuti umphawi udzacepa.

Cinanso ndi cakuti, ngati azimai adziwa za ufulu wosiyanasiyana, monga ufulu wokhala ndi zinthu zawozawo, ufulu wolankhula zakukhosi

ndiponso ufulu wopita kusukulu, iwo sadzapondelezedwa ndipo kupita kusukulu kudzawathandiza kudziwa zinthu zambili zimene zidzawatukula mu umoyo wawo. Paja onena amati; 'kuphunzitsa mwana wamkazi ndi kuphunzitsa dziko lonse'. Ici cimatanthauza kuti ngati mwana wamkazi waphunzila, anthu ambili adzathandizika cifukwa mkazi ndiye amene amasunga banja ndipo iye amadziwa zofunikila za ana onse akazi ndi amuna. Popeza akazi ndi amene amalima cakudya cambili, kupita kusukulu kudzawathandiza kudziwa njila za tsopano za ulimi ndipo dziko lidzatukuka.

MNDANDANDA WA ZOWELENGA

Chambers, J.K. 1995. *Sociolinguistic Theory*. Oxford: Blackwell.

Gwengwe, John .1994. *Chinyanja China*. Lusaka: Zambia Educational Publishing House.

Gyimah, A. 2009. *Gender and Transitional Justice in Western Africa: The Cases of Ghana and Sierra Leone*. Kenya: Nairobi ALC Report No. 4.

Human Development Reports. 2014. *What is Human Development?* United Nations Development Program, http://hdl.undp.olg/hd/

Katebe, Beauty. 2014. NGOCC Congratulates Newly Elected Female Participants. Zambia National Women's Lobby Press release. 12th September, 2014. Zambia: Lusaka.

Mhute, Isaac .2008. Language and Gender. In *Openspace. A Digest of the Open Society Initiative for Southern Africa*. Vol 2 (1) 60- 63.

Miti, L. M. 2002. *Kupa Ulemu Ŵanakazi*. Cape Town: The Centre for Advanced Studies of African Society (CASAS).

_____ 2008. Language Rights as a Human Rights and Development Issue in Southern Africa. In *Openspace. A Digest of the Open Society Initiative for Southern Africa*. Vol 2 (3) 7- 18.

Mutahhery, A. M.1992. *Woman and her Rights*. Accra: Islamic Seminary Publications.

Mwale, Engwase B. 2012. Gender Equality in Zambia. A Presentation On Gender Equality in Zambia held On 12-13 April, Cresta Golf View Hotel.

Ngalande, Sande. 2013. Nsenga Proverbs in Zambia: A Linguistic, Ethnographic and Logical Analysis. Japan: Kyoto University Phd Thesis: Upublished.

Olsson, Linda. 2000. A Study of Gender-Related Differences in Introductory Letters. C-Extended Essay.

Ross, Kalen. 2000. *Women Behaving Badly? Framing Gender in political communication*. Paper for political studies association - UK 50th Annual Conference, 10-13 April 2000, London.

Shuh, Anup (2010). *Women Rights*, Global Issues: http://www.globalissues.org/alticle/166/womensrights. 12/11/2013

Simango, Silvester. R. 2002. *Miyambo Yathu ndi Ufulu wa Amai*. Cape Town: The Centre for Advanced Studies of African Society (CASAS).

Simwinga, J. Does Language use Disadvantage Women? Seminar Paper presented at the University of Zambia, Lusaka, on 10th March, 2006.

Tiondi, T. 2001. *Women, environment and development: Sub-Sahalan Africa and Latin-America.* Theses and Dissertations. Paper 1549. http://scholarcommons.usf.edu/etd/1549

HIV and AIDS in Zambia: Zambia. 2012. Statistics. Avert.org/hiv-aids zambia.htm www.webdesignschoolguide.com/.../10 famous females.

MLEMBI

A Naomi Njobvu ndi aphunzitsi pa sukulu lalikulu la *University of Zambia* mcigawo ca zolemba ndi zilankhulo. Iwowa amaphunzitsa mmene anthu afunikila kulemba ndi kuyankhula bwino. Aphunzitsanso mmene aphunzi afunikila kumvetsetsa zolemba za anthu ena, ndinso mopangila mau ndi mmene mauwa amapangila ziganizo. Ali ndi cidwi kwambili kumafufuza pa nkhani zokhuza azimai ndi azibambo ndi mmene mau opangidwawo angasankhanitsidwe kuti apange ziganizo zoyenela. A Njobvu analinso aphunzitsi a Cingelezi ndi ciNyanja ku sekondale sukulu kumbuyoko pamene anayambayamba nchito mcaka ca 1997.